UNDUNA WA ZACHILENGEDWE

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

# NYENGO MSABATAYI

## KUYAMBIRA PA 4 MPAKA PA 10 MAY, 2026

## NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Tiyembekezere nyengo yamitambo yapatalipatali ndi yofunda m'madera ambiri, komanso nyengo yozizira nthawi ya usiku ndi m'mbandakucha kuyambira Lachiwiri pa 5 May mpaka pa 10 May 2026 kamba ka mphepo zomwe zidziomba kuchokera kumvuma. Chifunga chikuyembekeza muzigwa makamaka nthawi m'mbandakucha.

## NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kunali nyengo yamitambo yapatalipatali ndi yotentha m'madera ena komanso mvula makamaka m'madera a mphepete mwa Nyanja kuchigawo chakumpoto. Songwe Water Board station ku Karonga kunagwa mvula yochuluka yokwana **85.2mm** m'maola 24.

Mapu alimunsiwa akuonetsa m'mene mvula yopitilira mulingo wa 20mm inagwera kuyambira pa 27 mpaka pa 30 April 2026.





Figure 1: *Mapu akuonetsa mvula yochuluka yopitilira mulingo wa 20mm yomwe inagwa kuyambira pa 27 mpaka 30 April 2026*

## MALANGIZO M'SABATALI

- Pomwe nyengo yozizira ikupitilira, tikumbukire kuvala zovala zokwanira komanso tipewe kuotha mbaula mawindo ndi zitseko zili zotseka
- Kukakhala chifunga tikhale osamala panseu poyendetsa galimoto ndi njinga zamoto.

*__Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:__ The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 3 MAY, 2026**